## Mafunso pali za umfiti na ochilitsa

1. Pamene munakhuzidwa ndi zaufiti mu banja mwanu:

    a. Kodi cinakuthandizani nciani? Munathandizidwa bwanji? (Mu banja lanu kapena ndi munthu wina)

    b. Nciani cinakubweletsani pamodzi kapena cinakupatulani mu banja?

    c. Mpingo unathandiza motani? Kapena ni ciani munali kuyembekeza kucokera ku chalichi?

2. Pamene munali kuganiziridwa kukhala mfiti:

    a. Ndani anakuthandizani ndipo motani? (Mu banja lanu kapena ndi munthu wina)

    b. Mpingo unathandiza motani? Kapena ni ciani munali kuyembekeza kucokera ku chalichi?

3. Mupingo suvomeleza njila yowombeza kapena kukhulupirira mizimu. Kodi muganiza kuti ndizifukwa zotani?

4. Lamulo la dziko la Zambia siyivomeleza kugwira mfiti chifukwa cha kuombeza kapena kudzudzula za ufiti. Kodi muganiza kuti ndizifukwa zotani?

5. Kodi tingalimbikitse motani ng'anga kapena Akristu othandiza odwala / ophemperera odwala kuti aleke kukhulupirira kupeza mfiti?

6. Anthu ambiri amagwiritsa nchito mitundu ya mankhwala osiyana-siyana. Ena ndi ochiritsa koma ena ni oipa.

    a. Ndi mankhwala otani omwe inu mudziwa kuti ndi olodzela kapena akhudzana ndi ufiti?

    b. Kodi chimacitika nchiani ngati m'banja agwilitsa nchito mankhwala amenewa?

    c. Mpingo subvomereza mayele ngakhale a chikondi, chambu, chikoka cha za malonda kapena kukwezedwa pa nchito. Nchifukwa ciani?

    d. Kodi tingaletse bwanji anthu kugwilitsa nchito mankhwala amenewa?

7. Mpingo subvomeleza kucita za umfiti kapena kutengako mbali pa za umfiti munjila yili yonse. Kodi tingachite bwanji ndi anthu amene adziwika monga ali ndi mankhwala oipa kapena amachita poyera zokhuza zaufiti?

8. Ufiti umapezeka mu mabanja opatukana omwe muli chidani.

    a. Kodi mpingo ungathandize bwanji mabanja omwe muli chidani kuyanjana pomwe zinthu zisanavute, pomwe kuganizirana za ufiti sunafike poipa?

    b. Tingathandize bwanji mabanja opatukana kukambirana pa zokhuza za ufiti mu chalichi ndi chikulupiriro ndi ponso mu njira yothandiza munthu ali yense?

9. Pamene anthu amapita ku ng'anga amachita izi, abanja pamodzi ndi mutu wa m'banja amakonda kugwirizana ndi mwini mudzi. Kodi ndi thandizo lotani tingathandize ku kugonjetsa chidani ndi kusamala mtendere kopanda kuombeza olo kupita ku ng'anga?

10. Anthu ena oganiziridwa kukhala mfiti amavomera kuperekezedwa ku ng'anga pofuna kuti acite umboni wakuti alibe ufiti. Kodi tingawathandizire motani kuchotsa dzina la mfiti pa maso pa anthu popanda kuyenda ku ng'anga?

11. Panthawi ya matenda kapena ya umfiti akristu ambiri amakonda kupita ku maprophita ndi ku aneneri osiyana-siyana am'pingo ina m'malo mopita ku mpingo wao.

    a. Nchifukwa chiani?

    b. Kodi zotuluka zikhala zotani?

    c. Kodi mpingo ungalamule bwanji pali iyi nkhani?

12. Mpingo umafuna kukhala ochiritsa. Kodi tingathandiza bwanji mabanja omwe akhuzidwa ndi za umfiti?

13. Mfundo zina zomwe mungafune kuti mpingo ukuthandizeni ndi zotani?